**Nkhani zounikira za: Mark Thiesen, *Churches of Christ: A History of the Restoration Movement in Malawi 1906-1981* [Mipingo ya Khristu: Mbiri ya Gulu Lokonzanso ku Malawi 1906-1981]. Buku limafalitsidwa ku Mzuzu: Mzuni Press 2020 (mzunipress1@gmail.com), komanso ku London: African Books Collective 2020 https://www.africanbookscollective.com/books/churches-of-christ)**

Wounikira[1] Steven Paas

Monga mbale wogwira ntchito makamaka ku chigawo cha kum'mwera cha Malawi, Dr Mark Thiesen anagwira ntchito m'dziko lomwenso adakhala nthawi yambiri mu chinyamata chake. Iye adakhalanso ku chigawo cha kumpoto komwe makolo adali ofalitsa Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu (amishoni) a nthambi ya Mpingo wa Khristu (Church of Christ) ya ku Amereka. Chiyambi chake pa nkhani yophunzira za Umulungu komanso chikhalidwe chake zidathandizira kuti alembe buku la ukachenjede, lomwe lidachokera ku kafukufuku wake wa za Gulu Lokonzanso Mpingo (Restoration Movement) la ku maiko a Mgwirizano wa Mafumu (United Kingdom) ndi Amereka, makamaka pa kufika kwa Mpingo wa Khristu (Church of Christ). Ndi mutu wachiwiri. Mbali zina zonse za bukuli (mitu 3-7 ndi zowonjezera 1-8) ndi kafukufuku wozama wa kukula kwa Mpingo wa Khristu ndi migawikano yake yosiyanasiyana mu zaka za 1906 kufikira 1981.
Izi zachititsa kuti kafukufuku akhale wofunika powonjezera mbiri yosadziwika ya kubwera kwa Gulu Lokonzanso Mpingo makamaka pa kukula kwake ku Malawi.

Mwatsatanetsatane wolemba aonetsa mbali yamphamvu komanso ina yofooka ya gululi. Aonetsa momwe inafikira potchulidwa kuti 'Mpingo wa Khristu', komanso ponena kuti unakhazikitsidwa pa ngodya zitatu, zomwe ndi: (1) Zoonadi za Babulo; (2) Mgwirizano wa Akhristu onse; (3) Ntchito yoyalika Uthenga Wabwino (Umishoni). Ku mbali yake ya mphamvu gulu lagwira ntchito kwambiri, makamaka za ntchito ya uzimu komanso za kupanga kulongosola kwa ntchitoyi. Makamaka Mulungu anadalitsa ntchito za Akhristu a Chimalawi.
Pogwira ntchito limodzi ndi amishoni a Chizungu komanso polandira thandizo lawo, adakwanitsa kuitanira anthu ochuluka kwa Yesu, ndipo anamulandira kuti akhale Mpulumutsi wawo. Anthu a Malawi anathandizidwa ndi malo a za maphunziro, amene anagawana ndi nkhani yaifupi yosindikizidwa yokhudzana ndi za uzimu (mathirakiti a za Baibulo) ndi zina zolembedwa m'ziyankhulo za anthu a madera awo. Motero, ntchito yaikulu idagwiridwanso ndi Sukulu ya Baibulo ya Namikango ku Thondwe m'mboma la Zomba, yomwe nthawi zotsatirazo idayendetsedwa ndi wolemba bukuli. Zotsatira zake zinali zoti zinakula chiwerengero cha mipingo komanso cha okhulupirira a Khristu. Komabe

[1] Nkhaniyo yasindikizidwa ndi *Uthenga Magazine*, 21 September 2022, Uthenga Issue 3 2022.pdf (dropbox.com)

pamene Gulu Lokonzanso Mpingo limeneli lidasiya kusamala za mgwirizano wa ngodya zitatu komanso kulumikizana kwawo ndi Khrisitu mwini zofooka zake zidayamba kuonekera komanso kagwiridwe ntchito kake ka uzimu kadayamba kutsika.

Wolemba aonetsa mamembala ambiri a Mpingo wa Khiristu sadalabadire khumbo la Khiristu loti fuko lake la Akhristu lakhale umodzi. Motero, adafoketsa ngodya ya umodzi, pokonda ngodya ya choonadi mopitirira muyeso. Chotsatira chake chinali kuti ngodya ya choonadi cha Chibaibulo chidagwedemuka, chimene chidadzetsa kukula kwa dongosolo la maganizo a malamulo. Chochitika ichi chidagawa Mpingo m'magulu osiyanasiyana omwe adayamba kulimbana. Iwo adayamba kutenga ngati achikunja onse omwe adali asadabatizidwe munjira ya kumizidwa m'madzi komanso onse omwe sadali kutsatira maganizo awo a za ndondomeko za Chipangano Chatsopano. Poteropo, ngodya ya Umishoni idayamba kusalabadira udindo wake wa za anthu a zipembedzo zina ndi kusintha poyesa kutenga mamembala a mipingo yachikhristu ina.

Chimodzimodzi, Dr Thiesen afotokozera momwe mamembala a Mpingo Wa Khristu ku Malawi adayambira kutaya ngodya yawo ya Choonadi cha Chibaibulo. Pokhumudwa ndi kusowa kwa mawu omveka bwino m'Baibulo okamba za kayendetsedwe ka dongosolo la Mpingo, adayamba kusalabadira kwambiri pa maziko a Yesu Khristu a Mpingo, amene Mulungu avumbulutsa, nkuyamba kufunafuna mgwirizano ndi ena posatengera chikhalidwe cha Baibulo. Potsatira, ngodya yawo ya Umishoni zinafooka, ndipo inayamba kuoneka mofanana ndi ziphunzitso zosalabadira mawu a mu Baibulo a za dongosolo la Mpingo Wake. Motero anapanga umodzi ndi mipingo ina mosalabadira zosatsatira za uzimu, komanso adadzitangwanitsa pa zokambakamba zopanda phindu ndi osakhulupirira ndinso mamembala a zipembedzo zina.

Mpingo ndi wa Yesu Khristu. Iye ndi Mutu wa Thupi Lake, limene lili chiyanjano cha oyera mtima, ndondomeko ya thunthu ya okhulupirira owona opezeka mu nthawi zonse komanso malo onse. Komabe mbali zonse za kufooka kwa Gulu Lokonzanso Mpingo m'maonekedwe pansi pa mutu woti: 'Mpingo Wa Khristu' zikuonetsa kuti dzina lokongolali siliwonetseratu kulunzanitsika kwathunthu kwa Baibulo pakati pa miyambo yopangidwa anthu mu Mpingo ndi Mutu Mmodzi Weniweni wa Mpingo wa Mulungu.

Polingalira motsendera, wolemba bukuli akumemeza mbali zonse za Mpingo wa Khristu kuti zibwezeretse mulingo wa m'Baibulo. Tikuyenera kuphunzira kuti ngakhale Akhristu enieni sakhala oongoka mbali zonse. Ngakhale mwina mipingo imadzionera kulungama, siyowongoka kwathunthu. Komabe Mulungu amawonetsera chikondi ndi chisomo Chake potandaza chiweruzo Chake. Timafunikira chikhululukiro cha Ambuye ndi kuyeretsedwa ndi chiyero cha

Mzimu Woyera tsiku ndi tsiku. Ndinapeza chizindikiro cha mpingo wina cholembedwa m'chiyankhulo cha Chilatini: 'Nec tamen consumebatur', chimene limatanthauza: 'chitsamba [chili moto lawilawi] koma osapsa'(*Eksodo* 3:2). Chodabwitsa kwambiri mu mbiri ya chipulumutso ndi kudekha kwa Mulungu chifukwa cha chisomo cha Khristu posatengera zoperewera komanso machimo athu. Mwina uwu ndi uthenga wofunikira kwambiri wa Dr. Thiessen kuchokera mu kafukufuku wawo wabwino wa mbiri ya 'Mpingo wa Khristu'.

Mwa tsoka, makope a buku limeneli amene amatsindikiziwa ndi wofalitsa mabuku wa ku Malawi kuno sanadindidwe bwino. Komabe mabuku omwe amatsindikizidwa ndi kutumizidwa ku London amachititsa kaso. Mwachidule: Tikuvomereza buku la Thiesen kwambiri!

Yemwe akuwonanso nkhaniyi, Dr. Steven Paas ndi katswiri wa za Fiyoloje. (mbiri ya mpingo, umishoni) ndipo adali mbusa wa Church of Central Africa Presbyterian (CCAP). Adalembapo mabuku okamba za mbiri ya mpingo ku Afirika ndi Ulaya, za umishoni, za mawu a aneneri a za Israyeli, komanso anapanga mtanthauzira mawu wa Chichewa.




*Chikuto cha edishoni ya ku London*




*Chikuto cha edisioni ya ku Mzuzu*